

2 Timoteo : 3:8-17

**Mutu : Mau a Mulungu ndiwo mankhwalayopangitsa
kubwerera ku chikhulupiriro choona.**

Moni, moni kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero Ambuye afuna kutitsogolera ndi mau ake apa Yesaya 40:28, amene tipeza akuti, “Kodi iwe sunadziwe? Kodi sunamve? Mulungu wachikhalire, Yehova, Mlengi wa malekezero a dziko lapansi, salefuka konse, salema; nzeru zake sizisanthulika.”

Mupologalamu yapita ija, tinali kukambirana pa 2 Timoteo 3:1-12, pomwe timaunika za kuchoka pa choonadi m’masiku otsiriza. Ndipo lero pa 2 Timoteo 3:8-17, tiona nkhani yakuti mau a Mulungu ndiwo mankhwala ya kuchoka pachikhulupiriro choona.

8. Ndipo monga momwe Yane ndi Yambre amatsutsana naye Mose, kotero iwonso atsutsana nacho choonadi; ndiwo anthu obvunditsitsa mtima, osatsimikizidwapachikhulupiriro.

Tsono Yane ndi Yambre ndiwo maina ya anthu amatsenga, amene anapikisana ndi Mose pamaso pa Farawo. Ndiye pamene tiwerenga nkhani imene pa Eksodo 7, tipeza kuti satana ali ndi mphamvu

zochulukana ndithu ndipo kuti ndiye amayeseza zinthu za Mulungu. Nkhani ikuti Yane ndi Yambre, anali kupanga zozizwa mwa mphamvu ya Satana pamene Mose amapangazozizwa mwa mphamvu ya Mulungu. Ichi, ndichifukwa chake akuchenjeza pa 1 Yohane 4:1, kuti, “Okondedwa, musamakhulupirira Mzimu uli wonse, koma yesani mizimu ngati ichokera mwa Mulungu; popeza aneneri onyenga ambiri anaturuka kulowa m’dziko lapansi.” Tere, lero lino anthu ambiri tikupusitsidwa ndi kuona ngati zozizwa zambiri zikuchokerakwa Mulungu, koma pamene zikuchokera kwa Satana.

Ichi, ndichifukwa chake Paulo akunena kuti anthu masiku ano, akufanana ndi Yane ndi Yambre, chifukwa ali ndi maganizo oipa, amene anakana ndi kutaya chikhulupiriro choona.

9. Koma sadzapitirirapo; pakuti kupusa kwawo kudzaonekeratukwa onse, monganso kupusa kwa iwo aja.

Iyi, ndi nkhani ya kuchita chinyengo kudzera m’mphamvu ya Satana. Ndiye Paulo akunena kuti, pali nyengo yomwe anthu oipawaangaonetsere mphamvu yawo, koma sadzaloledwa kuchita zimenezi kwa nthawi yaitari. Chinyengo chawo chidzaonekerandipo

dziko lidzadziwa choonadi.Kutsimikiza kuti anthu oterewa akhoza kumalemekezeka ndithu, komanso akhoza kumanyenga ndi kusokeretsa anthu.Iwo, mwa nzeru ndi kuchenjera kwawo akhoza kumabisa choona cha momwe zimachitikira, koma pambuyo pake zimaoneka kuti ndi zopusa.

Wokondedwa anzanga apaulendo, pano tikutsindika kuti chinyengo chimene atumiki ena akuchita chimawalemekezetsa ndithu, kotero kuti anthu ochuluka akopeka mtima, koma asokeretsedwa.Taonani kuti anthu apusitsidwa ndi mau akuti, zinthu zidzakhala bwino mu mpingo ngakhalenso m'moyo wawo.Koma choyenera kudziwa ndi chakuti nthawi ikudza momwe anthu ena adzaona ndi kuzindikirabodzalo. Ndiye nkhani yonseyi ikuti, ilipo nthawi pomwe bodzasilidzapitilira, ndipo pali chitsimikizo chonse chakuti, choonadi ndicho chidzapambana. Tere Paulo pa 2 Atesalonika 2:7, akunena kuti, “Pakuti chinsinsi cha kusayeruzikachayambadi kuchita; chokhachipaliwomletsa tsopano, kufikira akamchotsa pakati.” Kutsimikiza kuti chinyengo chilipo ndithu pakali pano, koma ikudza nthawi pomwe chinyengo sichidzapitilira kuchitika.

10. Koma iwe watsatatsata chiphunzitso changa, mayendedwe, chitsimikizo mtima, chikhulupiriro, kuleza mtima, chikondi, chipiriro.

Paulo panoakuti Timoteo anali ndi mwayi wakukhala ndi Paulo pafupi ndipo kuti anaona moyo wake, ngakhale momwe anapirira masautso. Mwa chimenechi Paulo akumulimbikitsa Timoteo, kuti nayenso ngati wokhulupirira ayenera kulimbika ndi kupirira m'mayesero ndi m'masautso. Iyi, ndiyo nkhani yomwe Paulo anaifotokonzanso pa 2 Timoteo 3:14, pamene anati, "Koma ukhalebe iwe mu izi zimene waziphunzira, nutschimikizika mtima nawo podziwa amene adakuphunzitsa."

Tsono Paulo anaona zomwe zinayamba kuchitika nthawi imeneyo, kotero kuti anali kumulimbikitsa Timoteo kuti iye, ngati wokhulupirira ayenera kuyembekeza masautso. Iyi, inali njira imodzi yokonzekeretsa Timoteo.

11. Mazunzo, kumva zowawa; zoterezonga anandichitiram'Antiokeya, m'Ikoniya, m'Lustro, mazunzo otere ongandawamva; ndipo m'zonsezi Ambuye anandilanditsa.

Pano Paulo akupereka chitsanzo cha moyo wake kuti iye anamva zowawa ndi kuzunzika m'madera ambiri monga ku Antiokeya, Ikoniya ndi Lusto. Tsono mukumbukira kuti kunali ku Lusto kumene Paulo anamuponyamiyala ndi kumupha, koma Mulungu ndiye anamuukitsa. Tere, ndichifukwa chake akunena kuti Mulungu ndiye amene anamulanditsa. Kodi inu muli wokonzeka kulowa m'mazunzo ndi mayesero chifukwa cha Kristu?

12. Ndipo onse akufuna kukhala opembedza m'moyo mwa Kristu Yesu, adzamva mazunzo.

Pano ndifuna ndiyambe ndi mau ya mkulu wina wotchedwa Melvin Laird, amene pa msonkhano waukulu wachipani cha Republican ku America, ananena kuti, "Masiku ano m'dziko lapansi zinthu zikupitakoipa kotero kuti mkristu sakukondedwa ayi."

Tere, pano ndifuna kutsindika mau akuti lero, tikuona kukwaniritsidwakwa mau amenewa chifukwa chikristucheni-cheni komanso akristu eni-eni sakukondedwa ayi. Tikunenetsa kuti akristu olimba ndiwo ayamba kale kulipa mlandu woimapachikhulupiriro choona. Kodi inu chikhulupiriro chanu,

chikuopseza moyo wanu?Koma ngati sichingaopseze moyo wanu ndiye kuti inu muli kukondweretsa dzikoli.

13. Koma anthu oipa ndi onyenga, adzaipachiipire, kusokeretsa ndi kusokeretsedwa.

Poyamba ndifuna ndinene lamulo, lauchimo.Kutanthauza kuti ngati munthu akhala wosatembenuka mtima, ndiye kuti amakula pakuchita uchimo, kotero kuti amazamamuuchimowo.Mwachitsanzo ngati munthu ndi mfiti, amatamba, ndiye amafuna atazama kwambiri kuti amfiti anzake asamupeze.Koma tiyenera kunena kutikuzama muuchimo, sikuchitika tsiku limodzi, koma zimachitika pang'onopang'ono monga momwe inu mungakulire m'moyo wachikristu.

Ndiye nkhani yomwe tawerengayi, ikugwirizanandi lamulo la uchimo momwe, Timoteo samayenera kuganiza kuti mazunzo sangamufikire kapena kuti akhozamupitilira mwanjira yakuti anthu oipa, mwina akhoza kusintha kuzunzako ayi.Iye, amayenerakuyembekeza kuti anthu oipawo adzakhala akuzamapakuipa kwawo.Kunena kuti kuipakokudzakhalakukuipira-ipira.Ndiye pachifukwa chimenechi,

Timoteo amayenera kukhala wotsimikiza mtima kuti iye pamodzi ndi anzake onse wotembenuka mtima, adzakhala akuzunzika.

Tsono Paulo akutsindika kunena kuti anthu oipawo, adzapitilizakukopa anthu ena kuti agwe muuchimo mwanjira yowanyengerera. Iyi, ndi nkhani yachinyengo, momwe anthu adzapusitsidwapakukhulupirira zochita zawo ngati ndi zoona, koma pamene chilichinyengo.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone zomwe zikuchitikazo m'masiku athu ano. Taonani kuti malinga ndi ziphunzitso za zozizwaziliko masiku ano, anthu ambiri anyengedwa kotero kuti amakhulupirira zonse zimene zimachitikazo. Ndiye ndikofunika kubwerezanso kuti, “Musakhulupirire Mzimu uliwonse, koma yesani mizimu ngati ichokera mwa Mulungu: popeza aneneri onyenga ambiri anaturuka kulowa m'dziko lapansi” (2 Yohane 4:1).

Tsono nkhani ikupitirira kuti, iwo amene amabvomereza za chinyengo, ayenera kudziwa kuti amadzinyenga wokha. Kutsimikiza kuti anthu amene amakhulupirira zinthu zabodzazi amaganiza kuti bodzalikhoza kulowa m'malo mwachoonadi pamaso pa Mulungu. Kapena kuti akhoza kunyenga Mulungu, amene ayesa

mtima aye.Ndiye tikutsimikiza kuti anthu amene amayesetsa kunyenga anthu ena, ndiwo amene amanyengedwakotheratu.Kunena kuti monga anthu wotembenuka mtima, mwachisomo cha Mulungu amakulam'chidziwitso cha mau a Mulungu, momwemonso anthu oipa, kudzera mwanjira za Satana, amapitanakula m'njira zoipazo. Mau awa, akutsimikiza ganizo la mkulu wina, wotchedwa Alford, amene anati, "Mpata pakati pa kuwala ndi m'dima, m'malo mochepa, ukupitakakula." Tsono nkhani ikuthera pakuti anthu wokhulupirira za chinyengowa ndiwo amene akunyengedwa ndi mphamvu ya chinjokachokalamba, m'dierekezi ndiwo amene alimsinga zake kotero kuti adzalowanaye pamodzi m'nyanja yamoto. Kodi inu muumilirabe kukhulupirira za chinyengo?

14. Koma ukhalebe iwe mu izi zimene waziphunzira, nutsimikizika mtima nazo, podziwa amene adakuphunzitsa.

Tsopano taona chithunzi cha masiku otsiriza kuti, anthu amene asokeretsa ena, nawonsoamadzisokeretsa wokha. Koma mwina mwafunsa kale kuti, nanga mwana wa Mulungu akhoza kuchita chiyani? Yankho likuti, mankhwala amene angagonjetsem'chitidwe

wokhala m'dziko lachinyengo ndi mau a Mulungu basi.Ili, ndilo yankho lomwe Paulo analipeza, koterokuti akulimbikitsa mwana wake, Timoteo kuti akhalebemuzinthu zimene waziphunzira.Ndiye mwina mwafunsanso kuti, kodi Timoteo adaphunzira chiyani?Taonani iye anaphunzira mau a Mulungu kuchokera kuubwana wake, pamene agogo ake ndi amake, amene anali achiYuda, adaonetsetsa kuti Timoteo akukulam'chidziwitso cha mau a Mulungu.

Kutsimikiza kuti Timoteo samayenera kuchoka pa ziphunzitso za mau a Mulungu zimene analandira, pachifukwa cha kuzunzika kaya kunyengedwa ayi.Paulo akunena kuti popeza Timoteo anaphunzira mau a Mulungu osati monga momwe munthu amaphunzira maphunziro a science mwanjira yoyesa komanso mwamtendere, ayenera kuyesetsa kutenga udindo wosamalira ndi kusunga mauwo. Popeza ndiwo mau amene ali a ziphunzitsozoona, zimene sizitsutsana konse, zimene ndi zodzala ndi chitsimikizo ndi chiyembekezo cha moyo wangwiro. Ndiye Paulo akutsindika kuti chikhoza kukhala chinthu chochititsa manyazi kuti munthu

wodziwa chiphunzitso chokoma komanso choona, asiye ndi kutaya chiphunzitsochi.

Tsono Timoteo ayenera kugwiritsitsa choona chomwe anachiphunzira kuchokera kwa mtumiki wa Mulungu, amene ali Paulo mwini kuti munthu wina angalande. Pachifukwa chimenechi, Timoteo akulimbikitsidwa kukhala m'ziphunzitso zomwe analandira kuchokera kwa mtumiki, amene analandira ulamuliro kuchokera kwa Kristu mwini, amene utumiki wake wakhala ukuonetsa ndi kutsimikizika mwa zokoma ndi zozizwa zambiri. Iyi, ndiyo nkhani ija Paulo adanena pa 2 Timoteo 1:13, pamene adati, “Gwira chitsanzo cha mau a moyo, amene udawamva kwa ine, mwa chikhulupiriro ndi chikondi chiri mwa Kristu Yesu.” Komanso pa 2 Timoteo 3:15, Paulo akunena kuti, “Ndi kuti kuyambira ukhanda wako wadziwamalemboopatulika, okhozakukupatsa nzeru kufikira chipulumutso, mwa chikhulupiriro cha Kristu Yesu.” Ndiye Uthenga ndi wakuti popeza Timoteo adayamba kumva Uthenga Wabwino kuchokera kwa makolo ake, chiyenera kukhala chilimbikitso china chomwe ayenera kusunga ndi kugwiritsitsa mauwo. Izi, ziri chomwechi

chifukwa kholo la silingaphunzitse mwana wake chinthu chomwe adziwa kuti ndi chabodza. Kachiwiri, kholo ndiye munthu amene ali ndi chidziwitso chokwanira cha zinthu zoonā ndi zonama, popeza wayendamo m'moyo umenewu. Kachitatu tiyenera kukhala ndi chidziwitso chochitira makolo athu ulemu pazinthu zomwe akhala akuphunzitsa.

15. Ndi kuti kuyambira ukhanda wako wadziwamalemboopatulika, okhozakukupatsa nzeru kufikira chipulumutso, mwa chikhulupiriro cha mwa Kristu Yesu.

Mundime ino, ndifuna kugwira mau akuti “wadziwamalemboopatulika, okhozakukupatsa nzeru kufikira chipulumutso.”Tsono pano mwina mwafunsa kale kuti, kodi Paulo amatanthauza chiyani popeza Timoteo anali atapulumutsidwa kale?Yankho likuti chipulumutso chimachitika m'magawo atatu.Poyamba timaona chipulumutso chomwe tinalandira kale.Kachiwiri, timaona chipulumutso chomwe chikuchitika m'nthawi yatsopano ndipo Kachitatu timaona za chipulumutso chomwe chidzachitika m'tsogolo.

Tamvani kuti, ifetina pulumutsidwa kale pamene Ambuye Yesu anasenza zolakwa zathu pamtanda. Ndipo pamene tinakhulupirira ntchito imeneyi, tinachokakuimfa ndi kupita kumoyo kotero kuti “Ife wokhala mwa Kristu, Yesu tilibe kutsutsidwa” (Aroma 8:1). Ndiye m’nthawi yatsopanoife wokhulupirira timakhalatikupulumutsidwa. Kutanthauza kuti Ambuye Yesu, kudzera mwa Mzimu Woyera akutikonzabe tsiku ndi tsiku, koma tisanafikepoyeretsedwakwathunthu. Monga mwa mau apa 1 Yohane 3:2, amene akuti, “Okondedwa, tsopano tiri ana a Mulungu, ndipo sichinaoneke chimene tidzakhala. Tidziwa kuti pa kuoneka Iye, tidzakhala ofanana ndi Iye pakuti tidzamuona Iye monga ali.” Kutanthauza kuti mau a Mulungu samangopereka mwayi wotipulumutsaife tokha, koma kutipulumutsanso m’moyo watsiku ndi tsiku. Kunena kuti mau a Mulungu amatithandizaifekukula m’moyo wauzimu. Kutsindika kuti pamene inu ndi ine, tikhala ndi chizolowe zichosanthula mau a Mulungu tsiku ndi tsiku, amatipangaifekukulamwakutipatsa nzeru kufikira chipulumutso. Mau a Mulungu ndiwo amatipatsa nzeru momwe tingakhalire pansi pano, kufikira tikalandire chipulumutso m’tsogolo.

16. Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa chiphunzitso, chitsutsano, chikonzero, chilangizo cha m'chilungamo.

Pano ndiyambe ndi mau akuti, pamene Paulo akuti “lemba lili lonse,” akutanthauza mau a Mulungu kuchokera ku buku la Genesis kufikira Chibvumbulutso. Koma mwina inu mkufunsa kuti, kodi buku la Chibvumbulutso likhala lopatulika bwanji popeza bukuli linalembedwakalata iyi, yopitakwa Timoteo italembedwa kale?Yankho likuti mabuku onse amene analembedwakalata iyi, italembedwa kale, amene akutchulidwa kuti ndi mau a Mulungu, anauzilidwa ndi Mulungu mwakubvomerezedwa ndi mipingo momwe munali atumiki amene anali ndi Mzimu wachidziwitso. Kutanthauza kuti atumiki awa, anali ndi Mzimu amene anali kuwaunikira mau oona a Mulungu kusiyana ndi mau a munthu.Kutsindika kunena kuti mau onse ndi opindulitsa popeza Mulungu anauzira monga analenga munthu.Kutanthauza kuti anaikamo moyo m'mau onsewa.

Wokondedwa anzanga apaulendo, pano tikunenetsa kuti mau a Mulungu onse, amene tiyenera kuwadziwa ndi ochokera

kwaMulungu Woyera, amene anaperekedwa ndi atumiki oyera, ndi cholinga chofuna kupanga inu ndi ine, anthu oyera. Tikunena kuti awa, ndi mau oyera popeza ndiwo osiyana ndi mau ena, amene amangoona za chikhalidwe, koma sakhudza za chiyero cha munthu ayi.

Ndiye tikunenetsa kuti chinthu chimene chipambanitsa mau a Mulungu ndi chakuti mauwo ndiwo amene anauzilidwa ndi Mulungu. Ichi, ndicho chidziwitso chochokerakwa Mulungu, chimene inu ndi ine, tikhoza kuchidalira popeza chilibe cholakwa china chilichonse.Kutsimikiza kuti Mzimu wa Mulungu umene unauzira kapena kupereka nzeru kwa munthu, ndi Mzimu womwewo umene unapereka chidziwitso chapadera kwa ife. Iyi, ndiyo nkhani yomwe ikukambidwa pa 2 Petro 1:21, pamene akuti, “Pakuti kale lonse chinenero sichinadza ndi chifuniro cha munthu; koma anthu a Mulungu, ogwidwa ndi Mzimu Woyera, analankhula.”

Ndiye mwina inu mkufunsa kuti, kodi mau a Mulungu ndi wofunika bwanji kwa ife? Yankho likuti mau a Mulungu ndiwofunika popeza ndiwo amene amatipatsa nzeru za

chipulumutso.Kunena kuti mau a Mulungu ndicho chinthu chotitsogolera choona panjirayopitakumoyowosatha. Kutsindika kuti iwo amene ali anzeru, ndiwo amene ali anzeru kuchipulumutso cha moyo wawo. Mau a Mulungu ndiwo amatipanga kukhala anzeru ku mizimu yathu ndi kudziko lino.Ndipo ndikoyenera kudziwa kuti mau a Mulungu amapanga munthu kukhala wanzeru pamene aika chikhulupiriro ku mau a Mulunguwo.

17. Kutu munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kuchita ntchito iri yonse yabwino.

Tsono pamene Paulo akunena kuti mau a Mulungu amapanga munthu kukhala woyenera, sakunena kuti ndi wolungama kotheratu ayi, koma kuti amapanga munthu kukhwima m'moyo wachikristu.Koma tidzakulakweni-kweni ndi woyenera pamene tidzafika kwathu.

Tiyeni titsirize ndi mau akuti, mau a Mulungu ndiwo amene angakupangeni kuchita ntchito iri yonse yabwino. Kutsindika kunena kuti, ndimau a Mulungu wokha, amene angafikire ndi kukwanitsa chosowa cha mtima wa munthu. Pano tikunenetsa kuti pamene mau a Mulungu alowa mu mtima mwanu, amachita

chinthu china chake, chimene mabuku ena sangathe kuchita.Kodi
chozizwa ichi, chinachitika m'moyo wanu?

Kwalerotilekeza pano ndipo timasanthula 2 Timoteo 3:8-17, pomwe
timaona nkhani yakuti mau a Mulungu ndiwo mankhwala ya
kubwerera pachikhulupiriro choona.

Ambuye akudalitseni inu. Amen!